NYA_TTB_1090_SCRIPT

1 Yohane :1:5-7

Mutu : Mulungu ndiye kuunika

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero Ambuye atitsogolera ndi mau opezeka pa Afilipi 4:4, amene akuti, “Kondwerani mwa Ambuye nthawi zonse: ndibwerazanso kutero kondwerani.”

Mupologalamu yatha tinali kukambirana pa 1 Yohane 1:1-4, pamene timasanthula kuti,“Mulungu ndiye kuunika/kuwala.” Ndipo lero pa 1 Yohane 1:5-7, tipitiliza kuona kuti “Mulungu ndiye kuunika.”

5. Ndipo uwu ndi Uthenga tidaumvakwa Iye, ndipo tiulalikira kwa inu, kuti Mulungu ndiye kuunika ndipo mwa Iye monse mulibe mdima.

Poyamba tiyeni tigwire mau akuti “Mulungu ndiye kuunika ndipo mwa Iye mulibe mdima.”Apa, tikunena kuti Mulungu ndiye woyera ndipo mwa Iye mulibe kanthu mkamodzi konse kodetsa pamene munthu ndiye woipa. Uku, ndiko kusiyana kwakuru kumene kuli pakati pa Mulungu ndi munthu.Ndiye funso likuti, kodi phompho

lomwe lili pakati pa Mulungu ndi munthu, akhoza kulumikiza ndani? Uku, ndiko kudali kulira kwa Yobu 9:33, pamene adati, “Palibe wakutiweruza, wakutisanjika ife tonse awiri manja ake.” Yobu adaona kuipa kwa munthu ndi kulungama kwa Mulungu, ndiye amaganiza kuti palibe kuyanjanakwamtundu uliwonse, kotero kuti amalira wina wake amene angakhale pakati pa Mulungu ndi iye munthu wochimwa. Mwanjira ina Yobu anali kunena kuti iye ndi Mulungu amene ndi woyera, akhoza kuyenda pamodzi motani? Mwanjira ina Yobu anali kugwirazana ndi mneneri Amosi 3:3, yemwe adafunsa kuti, “Kodi awiri adzayenda pamodzi asanapanganiranetu?”

Tsono monga ndidanena koyambirira kuti buku lino lagawidwa m’magawo atatu, gawo loyamba likufotokonza kuti Mulungu ndiye kuunika, gawo lachiwiri limanena kuti Mulungu ndi chikondi ndipo gawo lachitatundilimenelimati Mulungu ndiye moyo.Ndiye mugawo lino, Yohane akufotokonza kuti Mulungu ndiye kuunika. Uku, ndiko kufotokonzerakwa dzina la Mulungu popeza kuunika ndiko kumanena za ulemerero wa Mulungu. Kunena kuti zinthu zonse kapena mau onse amene anamveka ndi aneneri kuchokera kwa

Mwana wa Mulungu, zikuonetsa kuti Mulungu ndiye kuunika.Ndiye Yohane akunena kuti monga dzuwa limaonetsa poyera zinthu za dziko, momwemo Mulungu amaonetsa zinthu zauzimu pokhala Iye chitsime cha nzeru, chiyero, kukongola, chimwemwe ndi ulemerero.Komanso Yohane akunena kuti monga zinthu zamoyo zonse zidalira kuwala kuti zikule, momwemonso moyo wauzimu udalira Mulungu kuti ukule. Ndiye monga Mulungu ali kuunika, momwemo Kristu ndiye kuunika kwanthawi yathu ino. Ichi, ndichimene akunena 1 Yohane 2:8, pamene akuti, “Ndikulemberaninso lamulo latsopano, ndicho chimene chiri choona mwa Iye ndi mwa inu; kuti mdima uli mkupita ndi kuunika koona kwayamba kuwala.”Ndiye pofuna kusiyanitsapakati munthu ndi Mulungu, Yohane akunena kuti mwa Iye mulibe mdima.Kunena kuti mwa Mulungu mulibe ngakhale dontho ndi limodzi lomwe la tchimo, mulibe cholakwa, kusadziwa, mulibe chosalungama, chodetsa ndi imfa yomwe. Yohane akunena ichi, popeza ndichimene adamva iye kuchokera kwa Kristu osati kudzera mwa mau chabe, koma mwakuchita monga mwa mauwo. Kutanthauza kuti zomwe Kristu anali kuchita m’thupi pansi pano, zinali kuonetsa kuwala kwa ulemerero wa Atate. Kutsimikiza kuti Kristu

mwini ndiye amene anali Mau a Mulungu.Kunena kuti Mulungu anali kulankhula kapena kupereka Uthenga kupyolera muzomwe Kristu anali kuchita.

Wokondedwa anzanga apaulendo, cholinga cha mau onsewa ndichakuti pamene tikumva Mau a moyo, kuchokera ku Mau amuyaya, tiyenera kuwalandiramokondwera ndi mtima umodzi ndi cholinga chakuti ife wokhulupirira tikhale nawo makhalidwe ofanana ndi Mulungu amene timutumikira. Kutsimikiza mau aja Mulungu mwini adanena pa Levitiko 11:45, pamene adati, “Pakuti Ine ndine Yehova amene ndinakukwezanikukuturutsani m’dziko la Aigupto, ndikhala Mulungu wanu; chifukwa chake mukhale oyera, popeza Ine ndine woyera.”Kunena kuti makhalidwe a Mulungu olungama, opandachiphena chilichonse, ndiwo akhale chilimbikitso chathu pamene timtumikira pakufalitsa Uthenga Wabwino.

Kutanthauza kuti ndichinthu choyenera kuti dziko lodetsedwa lino, likhale ndi atumiki amene akuimira Mulungu amene ndiye kuunika kweni-kweni. Tere ndi Ambuye Yesu yekha, yemwe adaonetsa ndi kutsegulira moyo wangwiro wa Mulungu m’dziko lino. Kunena kuti Mwana wa Mulungu m’modzi yekha, yemwe ali pachifukwato cha

Atate, ndiye amene adaonetsadi kuwala kwa Mulungu. Ndiye kuyenera kudziwika bwino kuti wokhulupirira ayenera kukonza njira zake ndi makhalidwe a moyo wake monga mwa lamulo la Mulungupamene ayenda m'mau a Mulungu,.Tsono pamene tinena za kuyenda mumdima, tikunena kuti munthu akuyendamkusadziwa, m'cholakwa ndi kuchita motsutsana ndi chiphunzitso cha chipembedzo choyera.

Ndiye Yohane akuti pali anthu ena amene amayesera kukhala ndi chisangalalo m'chipembedzochi; ndipo amayesa kukhala m'chiyanjano ndi Mulungu pamene moyo wawo siwachipembedzo choyenera, wamakhalidwe oipa ndi wodetsedwa. Kwa anthu otere Mtumwi Yohane akuti, ndiwo anthu onama.Iwowa amatsutsana ndi Mulungu popeza Mulungu alibe kukambirana kapena sakhala m'chiyanjano cha mtundu uliwonse ndi anthu wodetsedwa.Kodi kuunika kukhala m'chiyanjano chanji ndi mdima?Iwowa angodzinyenga wokha. Mwanjira ina akunena kuti iwo amene ayenda mkuwala, adzakhala m'chiyanjano ndi Mulungu, pamene alibe ubale wina uliwonse ndi Mulungu.

Tsono Yohane akunena kuti popeza iwo adamva kwa Ambuye Yesu nkhani yakuti Mulungu ndiye kuunika, Kristu anali kunena kuti monga Atate ali kuunika, Iyenso ndiye kuunika popeza munthu amene waona Atate, ndiye kuti waona Mwana. Kutsimikiza kuti palibe munthu amene akhoza kudza kwa Atate nakhala ndi moyo komanso m'chiyanjano ndi Iye, osadzera mwa Mwana wake ayi.Kutanthauza kuti munthu aliyense ndi wochimwa monga akunena Paulo pa Aroma 7:18, kuti, "Pakuti ndidziwa kuti m'kati mwanga, ndiko m'thupi langa, simukhala chinthu chabwino; pakuti kufuna ndiri nako, koma kuchita chabwino sindikupeza."Paulo akunenanso kuti mwa munthu simulibe chabwino chokha, koma kuti munthuyondiwosamvera Mulungu monga akutsimikiza pa Aroma 8:7, pamene akuti, "Chifukwa chisamaliro chathupichidana ndi Mulungu; pakuti sichigonja ku chilamulo cha Mulungu, pakuti sichikhoza kutero."Kutsimikiza kuti munthu akukhala m'dziko loipa, lomwe ndiloukira Mulungu.Koma ngakhale dziko liukire Mulungu chotani, munthu ndiwochimwa ndithu, kotero kuti ndiye wopulumutsidwa ndi chisomo cha Mulungu.Koma funso mkukhalapo kuti, kodi munthuyu akhoza kuyanjana ndi Mulungu chotani?Kodi ndi zotheka kuyenda naye Mulungu amene ndi

woyera?Tsono munthu wayesetsa kuti ayende ndi Mulungu pogwiritsa ntchito njira zitatu, pamene ziwiri mwa izozi, ndizolephera.

Tere njira yoyamba munthu amafuna kutsitsa Mulungu kuti afike pamsinkhu wake. Tamvani;

6. Tikati kuti tiyanjana ndi Iye, ndipo tiyenda mumdima, tinama ndipo sitichitachoonadi;

Tiyeni pano tigwire mau akuti, “Tikati kuti tiyanjana ndi Mulungu.” Ndiye pamau awa, tipeza kuti pali anthu ambiri amene amanena kuti ali m’chiyanjano ndi Mulungu, koma pamene sali m’chiyanjano. Awa, ndiwo anthu amene amadzitenga kuti ndiwo afanana ndi chikhalidwe cha Mulungu, kotero kuti amanena kuti alim’chiyanjano ndi Mulungu, popeza ndiwo amene amalandira moyo wawo kuchokera kwa Mulungu.Koma pamene amayenda mumdima wauchimo, kusadziwa ndi mkusakhulupirira. Kutanthauza kuti anthu amenewa ndiwo amene ali wosatembenuka mtima ndi akhungu, amene chidziwitso chawo ndicho chodetsedwa, kotero kuti samudziwa Mulungu kudzera mwa Kristu. Iwowa alibe chidziwitso chabwino, komanso samaona kuti ndiwo wochimwa ndi

kuopsa kokhalamuchimo, kotero kuti sam'dziwa Kristu ndi chiyero chake komanso ndi njira yachipulumutso. Awa, ndiwo alendo ku Mzimu wa Mulungu ndi ntchito za chisomo kotero kuti samvetsa choona cha mau a Uthenga Wabwino. Iwowa, amapitilira kulowa mumdima ndipo amakonda kukhala mumdimamo, osati kuunika ndi chikondi ayi.Kutsimikiza kuti ndiwo anthu amene akhala m'chiyanjano ndi uchimo kotero amakhala mosatekeseka, napitilira kukhala motere.Ndiye Yohane akunena kuti ngati anthu amenewa anganene akukhalam'chiyanjano ndi Mulungu ndiye kuti akunama chifukwa chakuti ndi zinthu zotsutsana ndipo ndizosatheka kuti m'dima ndi kuwala zikhale pamodzi.Ichi, ndichifukwa chakuti mau a Mulungu pa 2 Akorinto 6:14, akutsindika kunena kuti, "Musakhale omangidwam'goli ndi osakhulupira osiyana; pakuti chilungamo chigawana bwanji ndi chosalungama?Kapena kuunika kuyanjana bwanji ndi mdima?"Kutanthauza kuti ulamuliro wauchimo ukhala m'chiyanjano chanji ndi Mulungu?Popeza Mulungu ndiye kuunika ndipo onse amene atenga kuwala uku, ndiwo amene akhala m'chiyanjano ndi Iye.Ndiye Yohane akuti, alipo anthu ena amene sanena zoona ndipo sachita monga mau a Mulungu anena, kapena kuti sachita mokhulupirika ndi moona

mtima, awa ndiwo akristu onyenga, popeza samachita chomwe anena.Iwowa akadakhala kuti akunena zoona akadayenda m'kuunika osati mumdima ayi. Ichi, ndichimene akunena Yohane 3:21, pamene akuti, "Koma wochita choonadi adza kukuunika, kuti ntchito zake zionekere kuti zinachitidwa mwa Mulungu."Ndiye popeza anthuwa sachita chimenechi, sanena choona ndipo kuti amanama.Iwowa amanena zabodza kuti amakhala m'chiyanjano ndi Mulungu popeza Mulungu salowa paubale wina uliwonse kapena kuti sulumikizana ndi Mzimu umene siwoyera ayi.Kutsimikiza kuti zonse zimene munthu wonyenga achita, ndi zonama. Ndiye tikunenetsa kuti monga Mulungu ali wolungama, ifenso tiyenera kukhala woyera kuti tikhoza kukhala abwenzi ake.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tikunena kuti pamene tifuna kuchita choona, ndiye kuti tiyenera kuchita monga mwa choonadicho.Ndiye ngati inu simungachite monga mwa choonadi, ndiye kuti simungakhalem'Kristu. Tikunena kuti mwina inu ndinu m'modzi mwa anthu ameneasanalawe mtendere weni-weni ndi chimwemwe chokhalam'chiyanjano ndi Mulungu, koma mumangonena kuti ndinu abwenzi a Mulungu, ndipo

mumangodalira kuchita zinthu zooneka kunja, pamene simudalawe mtendere wa mumtima, umene chipembedzo choyenera chimapereka.Tere ndichifukwa chake masiku ano, tikumva zochita zauchimo, zodetsa zambiri pakati pa akristu.Ndiye ndifuna kunenetsa kuti, ngati inu mutsimikiza mtima kuyenda ndi Mulungu, ndiye kuti mukuyendadi m'kuunika.Momwemonso ngati mukusunga tchimo la mtundu uliwonse zikutanthauza kuti simukuyenda ndi Mulungu.Kutsimikiza kuti njira yoyeserakubweretsa Mulungu kufika pamsinkhu wathu, ndiyosatheka.

7. Koma ngati tiyenda mkuunika, monga Iye ali m'kuunika, tiyanjana wina ndi mnzake, ndipo mwazi wa Yesu Mwana wake utisambitsa kutichotsera uchimo wonse.

Pano tiyeni tiyambe ndi mau akuti, Mulungu ndiye kuunika ndipo ngati ife tiyenda m'kuunika zikutanthauza kukhala m'chiyanjano ndi Mulungu. Kristu ndiye chitsanzo chokoma, amene adayenda m'kuunika monga Yohane akunena pa 1 Yohane 2:6, kuti, "Iye wakunena kuti akhala mwa Iye, ayeneranso mwini wake kuyenda monga anayenda Iyeyo." Ndiye pamene tinena kuyenda m'kuunika

monga Iye ali kuunika, sikungotsanza mapazi ake chabe, koma kuonetsadi kuti ndinu ake a Mulunguyo. Tikunena kuti kuyenda m'kuunikakumaonetsa zinthu zitatu izi:

1) Kuyenda m'moyo wachiyero. Kunena kuti inu ngati mkristu muyenera kudziwika ndi moyo wangwiro wopanda chodetsa, pokhala inu nyali ya dziko lapansi.
2) Kachiwiri, inu pokhala mkristu, muyenera kuyenda m'choonadi; Kutanthauza kuti inu nthawi yonse muyenera kugwira choona, chomwe ndi chotsutsana ndi chikunja. Ichi, ndichimene Paulo akunena pa 2 Akorinto 4:6, pamene akuti, "Pakuti Mulungu amene anati, kuunika kudzawalakuturuka mumdima, ndiye amene anawalam'mitima yathu kutipatsachiwalitsiro cha chidziwitso cha ulemerero wa Mulungu pankhope pa Yesu Kristu."
3) Kachitatu; mkristu amene ayenda m'kuunika, ndiye amene amakhala ndi mwayi wosangalala chifukwa cha mtendere umene umapezeka mwa Mulungu, ndipo mtendere umenewu umapitansokwa abwenzi woona.

Mau onsewa akutsindika kuti ngakhale munthu sangafikepakuwalakweni-kweni, koma amalandira kuunika koona kwa Mulungu.pachimenechi, tikunena kuti mkristu woona ndiye amene ali ndi makhalidwe ndi machitidwe ofanana ndi Mulungu. Ndiye Yohane akunenetsa kuti pamene inu ndi ine, tikhala m'chiyanjano ndi Mulungu moona mtima, tikhalansom'chiyanjano ndi akristu anzathu. Mwanjira ina tikunena kuti popanda chiyanjano pakati pa Mulungu ndi munthu, sipangakhale chiyanjano pakati pa munthu ndi munthu mnzake. Kutsimikiza mau aja, apa verse 6, akuti, "Tikati kuti tiyanjana ndi Iye, ndipo tiyenda mumdima, tinama ndipo sitichita choonadi." Kutanthauza kuti akristu tikhala m'chiyanjano wina ndi mnzake pamene tikhala ndi makhalidwe ofanana ndi a Mulungu, akristu tonse tikhala ofanana wina ndi mnzake popeza tonsefetikonda Mulungu m'modzi ndipo tidalandira chipembedzo chimodzi, wokhala ndi cholinga chimodzi. Anthu okhala m'chiyanjano ndi Mulungu ndiwo anthu amene anamzindikira Mulungu ndipo analandira Mzimu wake, kotero amakhala ndi chithunzi cha Mulungu pamtima pawo.

Ndiye akunenetsa kuti onse amene akhala m'chiyanjano ndi Mulungu ndiwo amene mwazi wa Kristu utsuka machimo awo nthawi yonse popeza tikhala m'dziko lodetsedwa ndi mphamvu ya satana komanso kudzera mkufooka kwa matupi athu auchimo. Koma tiyenera kuzindikira kuti Yohane sakunena nkhani yakulungamitsidwa pamene mwazi wa Kristu utsuka ndi kuchotsa chosalungama ayi. Iye akunena za kuyeretsedwakwa moyo tsiku ndi tsiku wachikristu. Kutsimikiza kuti ngati pali chinthu china chomwe mkristu amalandira kwa Mulungu m'moyo uno, ndicho chiyanjano ndi Mulungu ndi akristu anzake komanso kuyenda m'kuunika, chinthu chomwe sichiperekedwa kwa munthu wosayenda m'kuunika. Tere ndichifukwa chake Mtumwi Yohane akunena kuti, "Tikati kuti tiribe uchimo, tidzinyenga tokha ndipo mwa ife mulibe choonadi."

Tsono nkhani ikunena kuti ndizotheka kuti inu ndi ine, kuyenda m'kuunika pamene tilola kuti mwazi wa Kristu utiyeretse ndi kutichotsera zosalungama zathu zonse. Kutsindika kuti mwazi wa Kristu ndiye sopo amene amakhozakuyeretsa tchimo la mtundu uliwonse pokhala anthu amene tinalungamitsidwa kale.

Kutanthauza kuti ngati sitingalapendikulola kuti mwazi wa Ambuye Yesu Kristu, utsuke ndi kuchotsa tchimo ndiye kuti tchimolo liononga chiyanjano chonse ndi Mulungu.

Kutanthauza kuti pamene tifikapozindikira tchimo lomwe lili m'moyo mwathu, muli mphamvu m'mwazi wa Kristu yochotsachosalungama ndi kutipanga ife wolungama. Kutsimikiza kuti palibe chodetsa chomwe sichingachoke m'moyo mwathu ndi mwazi wa Kristu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna titsirize ndi mau akuti, nkhani yonseyi ikugwirizana ndi mau aja ali mu verse 5, amene akuti "Mulungu ndiye kuunika ndipo mwa Iye monse mulibe mdima." Kunena kuti chipembedzo cha Mulungu uyu, chimafuna anthu onse amene ndiabwezi ake, akhale ofanana ndi Iye (Mulungu) pakuyenda m'kuunika.

Ndiye ndifuna mumvetsetse kuti Mulungu pankhani ya kuyenda m'chiyanjano ndi Iye, akuitenga pa chithunzi cha m'banja. Iye akunena kuti pamene mwana wa m'banja achita choipa, amakhala mwana ndithu koma amatchedwa mwana wosamvera. Apa, ndipo pamene mwana uyu, amataya chiyanjano chake ndi atate wake.

Momwemonso inu, ngati mkristu mukachita choipa, moyo wanu umadetsedwa ndi tchimo, kotero kuti mumataya chiyanjano chanu ndi Mulungu komanso ndi akristu anzanu.Kodi muli wokonzeka kuyanjana ndi Mulungu lero?

Kwalerotilekeza pano ndipo tinali kusanthula 1 Yohane 1:5-7, momwe timapitiliza kuona kuti “Mulungu ndiye kuunika.”

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!